



MAUBWINO 21

A KUSALA MASIKU

6

A SHAWW AAL

محرم صياح المجد

Wolembe: Sheikh
Saleh Al-Munajjid

Womasulira
Ramadhan Isa

*Maubwino 21 a Kusala Masiku 6 a Shawwaal
Sheikh Muhammad Salih Al-Munajjid*

M'dzina la Allah, Wachifundo Chambiri, Wachisoni Chosatha
Ufulu wonse wa kutsindika ndi kufalitsa bukuli ndiwa Msilamu aliyense

Kutamandidwa konse nkwa Allah, Mbuye wa zolengedwa zonse. Mtendere ndi Madalitso zikhale pa Mtumiki wa Allah salla Allah alaih wasallam.

Awa ndi maubwino, komanso kulongosola mwachidule kwa zambiri zokhudza kusala masiku 6 a mwezi wa Shawwaal, monga miyambo ndi malamulo. Tikumpempha Allah kuti aipange ntchitoyi kukhala yothandiza, komanso awalipire zabwino onse omwe athandiza kukhonza ndi kufalitsa Maubwino amenewa.

~ Muhammad Salih Al-Munajjid ~



1

Shawwaal ndimwezi wodalitsika, ndimwezi wa kumvera, komanso ndimayambiro a myezi ya Hajj, mmenemo muli kusala kwa masiku 6, kubweza I'tikaaf kwa amene inamudutsa, komanso ndimwezi womwe kukhalira pamodzi am'banja kumakhala halal.

2

Msilamu ndiwolamulidwa kusala masiku 6 a mu Shawwaal pambuyo pa Ramadan, imeneyi ndi Sunnah yokondedwa koma si waajib (sizokakamizika), ubwino wake ndiwaukulu ndipo malipiro ake ngaakulu.

3

Yemwe wasala masiku 6 a Shawwaal pambuyo pa Ramadan, amalembredwa malipiro a kusala chaka chatunthu, monga mmene Mneneri salla Allah alaih wasallam anenera:

"مَنْ صَامَ رَمَضَانَ، ثُمَّ أَتْبَعَهُ سِتًّا مِنْ شَوَّالٍ؛ كَانَ كَصِيَامِ الدَّهْرِ"

"Yemwe wasala Ramadan, kenako ndikutsatiza masiku 6 a mu Shawwaal, akhala ngati wasala chaka chonse".¹

4

Mawuwa Mtumiki salla Allah alaih wasallam anawalongosola ponena kuti:

"مَنْ صَامَ رَمَضَانَ فَشَهْرٌ بِعَشْرَةِ أَشْهُرٍ، وَصِيَامُ سِتَّةِ أَيَّامٍ بَعْدَ الْفِطْرِ (بِشَهْرَيْنِ)، فَذَلِكَ تَمَامُ

صِيَامِ السَّنَةِ: ﴿مَنْ جَاءَ بِالْحَسَنَةِ فَلَهُ عَشْرُ أَمْثَالِهَا ۖ وَمَنْ جَاءَ بِالسَّيِّئَةِ فَلَا يُجْزَىٰ إِلَّا

مِثْلَهَا وَهُمْ لَا يُظْلَمُونَ﴾

"Yemwe wasala Ramadan, mwezi umodzi ndiye kuti myezi 10, ndipo masiku 6 a Shawwaal ndiye kuti myezi iwiri, zomwe zikukwanitsa chaka chatunthu cha kusala,

¹ Sahih Muslim (1164)

"Amene wachita chabwino alipidwa zabwino khumi zofanana ndi icho. Ndipo amene wachita choipa sadzalipidwa koma chonga icho (popanda kuonjezera). Ndipo iwo sadzaponderedwa."^{1 2 3}

5

Ena akafunsa kuti: Kusala masiku 6 a Shawwaal kumaonjezera zabwino khumi monga mmene zabwino zimaonjezera nthawi zonse, nanga kufunika kwa kusalako ndikuti?

Yankho ndiloti: Ozindikira malamulo a Chisilamu ochokera mu madh'hab a Hanaabilah ndi Shafi'iya analongosola kuti kusala masiku 6 pambuyo pa Ramadan kumakhala ngati wasala chaka chatunthu kwa faradh.

6

Kuchokera mmaubwino a kusala masiku 6, tikupeza kuti muli kubwezeretsa kupunguka komwe kunachitika pakusala kokakamizika mu Ramadan, monga mmene ziliri mu Hadith iyi:

"إِنَّ أَوَّلَ مَا يُحَاسَبُ بِهِ الْعَبْدُ يَوْمَ الْقِيَامَةِ مِنْ عَمَلِهِ صَلَاتُهُ فَإِنْ صَلَحَتْ فَقَدْ أَفْلَحَ وَأَنْجَحَ وَإِنْ فَسَدَتْ فَقَدْ خَابَ وَخَسِرَ، فَإِنْ انْتَقَصَ مِنْ فَرِيضَتِهِ شَيْءٌ قَالَ الرَّبُّ عَزَّ وَجَلَّ: انظُرُوا هَلْ لِعَبْدِي مِنْ تَطَوُّعٍ فَيُكَمَّلَ بِهَا مَا انْتَقَصَ مِنَ الْفَرِيضَةِ؟ ثُمَّ يَكُونُ سَائِرُ عَمَلِهِ عَلَى ذَلِكَ"

"Ndithu choyamba chomwe kapolo adzawerengeredwe tsiku la Qiyaamah ndi mapemphero ake (swalaat), ngati idzakhale yabwino ndiye kuti adzasangalala

² Al-Imâm Ahmad (22412), Ibn Maajah (715), Ibn Khuzaymah (2115) – Sahîh Al-AIbaani

³ Sûrat Al-An'aam (160)

*ndikupambana, ndipo ngati idzakhale yoonongeka ndiye kuti adzakhala wolephera ndi kutaika. Ngati mu swalat yake yokakamizika mudzapezeka kupelewera, Allah Azza wa Jalla adzalamula kuti ayang'ane ngati kapolo wake anagwirapo ntchito inayake mongodzipereka, kuti ikwaniritse kupunguka kwa swalat yokakamizikazo. Kenako ntchito zake zonse zidzakwaniritsidwa moteromo.'*⁴

7 **Kuchokera kwa ma ulamaa ena, zinanenedwa kuti kusala masiku 6 a Shawwaal sikwabwino, ndipo anapereka vuto loti: kuopera kuti ena angakhulupilire kuti kumeneko ndikusala kwa mu Ramadan.**

8 Koma vuto limenelo silingagonjetse Sunnah yoona, ndipo Sunnah ndiyomwe tikuyenera kutsatira, isasiyidwe chifukwa cha mawu amunthu aliyense.

9 **Kuyamba kubweza faradh ndikwabwino kwambiri chifukwa kumampatsa munthu ufulu wake:** choncho yemwe ali ndi masiku omwe anamasula mu Ramadan chifukwa cha vuto, afulumire kubweza, kuti apeze ufulu; kumeneko ndiko kuyamba kwa kuchita zokondedwa.

Yemwe akufuna thawaab zomwe zatchulidwa mu Hadith ija, akuyenera kubweza masiku omwe anamasula mu Ramadan, kenako atsatize masiku 6 a Shawwaal, chifukwa kuyankhula kwa Mtumiki salla Allah alaih wasallam koti: ثُمَّ أَتْبَعَهُ سِتًّا مِنْ شَوَّالٍ؛ kukusonyeza

⁴ Abu Dâwud (864), Al-Tirmidhi (413) – Sahih Al- Albaani

kuti ndithu munthu akuyenera ayambe kukwaniritsa swawm yake ya Ramadhan, kenako asale masiku 6, "chifukwa sizingaloledwe kwaiye kutsatidza kusala masiku 6 a Shawwaal pambuyo pa Ramadan, pokhapokha atakwaniritsa swawm yake".⁵

10

Sizololedwa kuphatikiza Ramadhan ndi masiku 6 a Shawwaal pa niyya imodzi. Yemwe wamasula chifukwa cha vuto ndipo wayamba kubweza, sakuloledwa kuphatikiza swawm ya masiku 6 a Shawwaal ndi kubweza kwake kwa masiku a Ramadan pa niyyah imodzi.

11

Ndizololedwa osala masiku 6 a Shawwaal kusala mondondoza masiku 6, kapena kulekanitsa (kusala modumphitsa-dumphitsa) koma m'mwezi wa Shawwaal womwewo. Akhonza kusankha mmene akuonera kuti akwanitsa, ngakhale atachedwetsa palibe vuto, makamaka yemwe amamubwelera alendo pakhomo, kapena akusonkhana pamodzi ndi abale ake tsiku la Eid mpaka pambuyo pake...

12

Ndizololedwa kuphatikiza kusala kwa masiku atatu oyera komanso lolemba ndi lachinayi, ndi kusala kwa masiku 6 a Shawwaal pa niyyah imodzi. Ndipo ayembekezere kupeza malipiro awiri.

Kumeneko ndikusankha kwa Sheikh athu Abdul Aziz bun Baaz (Allah awachitire chisoni), iwo anati: "Ayembekeze zimenezo, chifukwa ndizoona kuti wasala masiku 6

⁵ Fatawa Al-Lajnatu Ddaaimah (10/392)

komanso ndizoonā kuti wasala masiku oyera, ndipo zabwino wa Allah ndi zochuluka."

"Ndizoonā yemwe wasala masiku 6 ndiye kuti wasalanso masiku atatu a pamwezi." *Ibn Uthaimin*

13

Kusala kwa masiku 6 a Shawwaal ngati kwagwirizana ndi tsiku loweruka; kukhala kusala kwake (kwa masiku 6), chifukwa sikuti wasala ndicholinga cha loweruka, koma wasala ndicholinga chakuti masiku 6.

14

Yemwe ali ndi masiku obweza mu Ramadan ndipo kusala kwakeko kwatenga mwezi wonse wa Shawwaal, monga mai yemwe ali mu nifaas (wangobereka kumene), adzasale masiku 6 a Shawwaal mu Dhil Qa'dah, ndipo adzapeza malipiro chimodzimodzi yemwe wasala mu Shawwaal; poti choti kucedwetsa kwakeko kunachitika chifukwa cha vuto lomveka. Monga mmene ananenera Sheikh athu Ibn Uthaimin (Allah awachitire chisoni), komanso zomwezo anayankha Sheikh Ibn Sa'di (Allah awachitire chisoni).⁶

15

Yemwe ali ndimasiku angongole ndipo sanabweze mu Shawwaal popanda vuto, sali oyenera kusala mu Dhil Qa'dah, ndipo sapeza malipiro aliwonse ngati angatero, chifukwa Sunnayo yadutsa nthawi yake yomwe inaikidwa popanda kupezeka ndi vuto.

16

Kuchokera muzikhulupiliro zolakwika: anthu ena amakhulupilira kuti yemwe wasala masiku 6 mu

⁶ Majmoo' Fataawa Ibn Uthaimin (20/19) - Al-Fatawa Al-Sa'diy (p.230)

Shawwaal, akuyenera kumasala chaka chirichonse (6 Shawwaal) ndipo isamamudutse! Zoona ndizoti kusala masiku 6 ndi Sunnah, yemwe wafuna asala ndipo apeza malipiro; sizokakamizika kuti yemwe wasala chaka chinachake, kapena zaka zochuluka, ndiye kuti azipitiriza. Koma yemwe wasiya chaka chinachake osasala samapeza machimo.

17

Anthu ena amakhulupilira kuti yemwe wayamba kusala masiku a Shawwaal ndiye kuti akuyenera kumaliza mpaka masikuwo akwane! Zimenezo sizooona, chifukwa Hadith ikunena kuti: "Yemwe akusala mongodzipereka ndi mtsogoleri wayekha; ngati wafuna asala, ndipo ngati wafuna amasula."⁷

Choncho osala ali ndi ufulu wa kudukiza swawm yongodzipereka, pamene ali ndi vuto ngakhale pamene alibe vuto, ndipo sakuyenera kubweza. Koma thawaab zomwe zatchulidwa mu Hadith zija sazipeza mpaka atakwaniritsa masiku 6.

18

Imodzi mwa ma bid'ah omwe alibe kochokera Mchisilamu: Anthu ena amasangalalira tsiku la 8 Shawwaal chifukwa cha kukwaniritsa kusala masiku 6, ndipo chisangalalo chimenechi amachitcha kuti "Eidul Abraar (Eid ya Ochita zabwino)"!

Sheikhul Islam Ibn Taymiya (Allah awachitire chisoni) anati: Tsopano pa 8 Shawwaal, limeneli si tsiku la eid kwa ochita zabwino ngakhale kwa ochita zoipa, ndipo

⁷ Al Imaam Ahmad (26893), Al-Tirmidhi (732) – Sahih Al-Albaani

sizololedwa kwa aliyense kukhulupilira kuti imeneyo ndi eid, komanso asachite chilichonse chokhudzana ndi eid.
Al-Ikhtiyaaraatil 'Ilmiyya.

19

Komanso ina mwa ma bid'ah: Kutaya mtima komanso kukhala ndi chikaiko pabanja m'mwezi wa Shawwaal. Ma Arab anali kutaya mtima pazakumangitsa banja m'mweziwu, chifukwa anali kukhulupilira kuti mkazi amakana mwamuna wake m'mwezi umenewu, monga mmene bulu wamkazi amakanira akakumana ndi bulu wamwamuna ndipo amanyamula mchira wake!

Mtumiki salla Allah alaih wasallam anaphwanya chikhulupiliro chimenechi pomukwatira Aaisha radhia Allah anha mu Shawwaal ndipo anayamba kukhala naye mu Shawwaal.⁸

20

Ndizokonedwa kukwatira komanso kukwatitsa (mwana wamkazi) mu Shawwaal; potengera Mtumiki salla Allah alaih wasallam, komanso kukana chikhulupiliro cha kutaya mtima kwa anthu a m'nthawi ya umbuli, pa zakusatheka kwa banja m'mweziwu, makamaka chikhulupiliro chimenechi chikakhala kuti ndichofalikira m'dera lathu. Mai wa okhulupilira, Aaisha radhia Allah anha anali kukonda kulowetsa azimai ake m'mwezi umenewu⁹.

21

Zina mwa zopeka: Chikhulupiliro cha anthu ena choti omwe akwatira pakati pa ma eid awiri (Eidul Fitr ndi Eidul

⁸ Sahih Musli (1423)

⁹ Sahih Muslim (1323)

Adh'ha) amwalira mmodzi wa iwo, kapena akhonza kulekana banja!

Chikhulupiliro ichi palibe komwe chikuchokera mu deen yathu, komanso kumeneku ndikudzipanga kuti akudziwa zobitsika zomwe palibe yemwe akuzidziwa koma Allah, ndipo kumeneku ndikuyankhula zoipa pa chikhulupiliro komanso chikhonzero. Kukaika kapena kutaya mtima ndikoletsedwa. Ndipo kuyamba kwa kukhala kwa Mtumiki salla Allah alaih wasallam pamodzi ndi Aaishah radhia Allah anha m'mwezi wa Shawwaal, kukuphwasula bodza limeneli.

*Tikumpempha Allah atilandire ntchito zathu, ndi kuti
atithandize pakumukumbukira Iye ndi kuchita zabwino
mmapemphero ake.*

*Kutamandidwa konse nkwa Allah, Mbuye wa zolengedwa
zonse*

